


Buku labwino kwambiri lachidziwitso choyambirira cha Chisilamu kwa oyamba kumene

ZIPHUNZITSO ZA CHISILAMU ZOYAMBIRIRA (GAWO LOYAMBA)



- Buku lopambana la ana pa zidziwitso za chisilamu zoyambirira.

Ziphunzitso zoyambirira za Chisilamu

(Gawo loyamba)

Wolemba:

Majlis Madrasa-tul-Madinah ndi Majlis
Al-Madina-tul-'Ilmiyyah

Womasulira m'chichewa:

Majlis-e-Tarājim Dawat-e-Islami

Wosindikiza bukuli:

Maktaba-tul-Madina Bab-ul-Madina, Karachi

الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَيْكَ يَا رَسُولَ اللَّهِ وَعَلَىٰ آلِكَ وَأَصْحَابِكَ يَا حَبِيبَ اللَّهِ

Dzina la bukuli:

Ziphunzitso zoyambirira za chisilamu (Gawo 1)

Wolembe:

Majlis Madrasa-tul-Madinah ndi Majlis Al-Madina-tul-'Ilmiyyah

Womasulira m'chichewa:

Majlis-e-Tarajim

Chaka chomwe bukuli linatsindikizidwa:

Jumadal Aakhir 1439 AH, March, 2018

E.mail:

Ilmia@dawateislami.net

Kufotokozero

Buku la ziphunzitso za chisilamu gawo loyamba lomwe linalembedwa mu Urdu' **Madani Nisab ya Madani Qaidah** (linasindikizidwa ndi Maktaba-tul-Madina) ndipo Majlis Taftish-e-Kutub-o-Rasail (Dawat-e-Islami) anawunikira bwino lomwe bukuli. Majlis Tarajim linamasulira buku lo unikiridwa bwinobwino la mu Urdu ndikuliika m'Chichewa.

Umwini:

Womwe ali woyenera kusindika bukuli ndi Maktaba-tul-Madina ndipo ena onse sakuloledwa kutero.

Zamkatimu mwachidule

Azkār 6

Kalimāt (ndemanga za chikhulupiro) 7-8

Ma Dua 9-11

Zikhulupiro 12-26

Machitidwe a kulambira 28-33

Ngale za Madanī 34-37

Makhalidwe 38

Miyezi ya Madanī 39

Dawat-e-Islami 40

Manqabat-e-'Aṭṭār 41-42

Mapemphero 43-44

Manqabat Ghauš-e-A'ẓam رضى الله عنه 45

Munājāt 46

Ṣalāt-o-Salām 47-48

Du'ā 49-50

Zonse za mkatimu zaikidwa kumapeto kwa bukuli.

Ndandanda wa Kafananidwe ka zilembo

ء	A/a	ژ	Ř/ř	ل	L/l
ا	A/a	ز	Z/z	م	M/m
ب	B/b	ژ	X/x	ن	N/n
پ	P/p	س	S/s	و	V/v, W/w
ت	T/t	ش	Sh/sh		
ٹ	Ṭ/ṭ	ص	Ş/ş	ة / ه / ه	Ĥ/ĥ
ث	Š/š	ض	Ḍ/ḍ	ی	Y/y
ج	J/j	ط	Ṭ/ṭ	ے	Y/y
چ	Ch	ظ	Ẓ/ẓ	ِ	A/a
ح	H/h	ع	‘	ُ	U/u
خ	Kh/kh	غ	Gh/gh	َ	I/i
د	D/d	ف	F/f	وِ	Ū/ū
ڈ	Ḍ/ḍ	ق	Q/q	یِ	Ī/ī
ذ	Ẓ/ẓ	ک	K/k	اِ	Ā/ā
ر	R/r	گ	G/g		

أَلْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى سَيِّدِ الْمُرْسَلِينَ
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ ط

Al-Madīna-tul-‘Ilmiyyah

Kuchokera kwa: Shaykh-e-Ṭarīqat Amīr-e-Ahl-e-Sunnat, Muyambitsi wa bungwe la Dawat-e-Islami, ‘Allāmah Maulānā Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi Ziyai دَاعَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَهُ

الْحَمْدُ لِلَّهِ عَلَى إِحْسَانِهِ وَبِفَضْلِ رَسُولِهِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

Dawat-e-Islami, bungwe la padziko lonse lapansi komanso losagwirizana ndi ndale lolalikira za Qur’an ndi Sunnah, ndipo latsimikiza kutsitsimutsa Sunnah ndikufalitsa chilungamo komanso chidziwitso cha Shari’ah padziko lonse lapansi. Pofuna kugwira ntchito yayikulu ndi yofunika kwambiri mu njira yabwino, Majalis angapo apangidwa kuphatikiza Majlis ‘Al-Madīna-tul-‘Ilmiyyah’ yomwe ili ndi ma Ulamā ndi ma Mufti a Dawat-e-Islami. Ma Majalis awa ali ndi chidwi chofuna kutumikira chipembedzo pankhani ya chidziwitso, kufufuza ndi kufalitsa. Bungweli lili ndi nthambi zisanu ndi imodzi zotsatirazi:

Nthambi ya ma buku a A’lā Ḥaḍrat رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ

- ❖ Nthambi yophunzitsa ma buku.
- ❖ Nthambi yokonzanso ma buku.
- ❖ Nthambi yomasulira ma buku.
- ❖ Nthambi yowunika ma buku.
- ❖ Nthambi yopereka umboni ndi kulemba.

Cholinga chenicheni cha Al-Madīna-tul-‘Ilmiyyah; ndikupereka ma buku a mtengo wapatali a A’lā Ḥaḍrat, Imām-e-Ahl-e-Sunnat, wotsitsimutsa Sunnah, wothetsa

Ziphunzitso za chisilamu zoyambirira

Bid'ah, wophunzira Sharī'ah, 'Allāmah Maulānā Al-Hāj, Al-Qārī, Ash-Shāh Imām Aḥmad Razā Khān رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ munjira yosavuta kumva molingana ndi zokhumba za m'bado uno. Abale ndi Alongo Achisilamu akuyenera kuzipereka kwa thunthu pakutukula ntchito za Madani, Pa chidziwitso, kafukufuku ,kusindikiza ,kuwerenga buku lililonse losindikizidwa ndi Majlis komanso kuwakopa ena kuchita chimodzimodzi.

Nthambi zonse za Dawat-e-Islami kuphatikiza Al-Madīna-tul-'Ilmiyyah zipite patsogolo (Allah) عَزَّوَجَلَّ atipatse chipambano pamoyo wathu wa padziko lapansi komanso m'moyo omwe uli mkudza, potithandizira kuchita zabwino zonse moona mtima. Tiyeni tonse tidalitsidwe pofera pansi pa dome yobiriwira, ndikuyikidwa m'manda ku Jannat-ul-Baqī' ndi kukhala ku Jannat-ul-Firdaus.

آمِينَ بِجَاهِ النَّبِيِّ الْأَمِينِ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

Matamando ndi ubwino wake

Sayyidunā Imām 'Abdullāh Bin 'Umar Bayḍāwī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ (yemwe anamwalira m'chaka cha 685 A.H.) anati, 'Yemwe amvera Allah عَزَّوَجَلَّ ndi Mtumiki wake Wokonededwa صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ, atamandidwa mu dziko lapansi ndipo adzapeza cholowa moyo omwe uli nkudza.' (TafsīrBaghwī, Gawo 22, SūrahAl-Hazāb, Taḥat-ul-Āyah71, Verse 4, samba. 388)

Chiyambi

Buku loyera la Qur'an ndibuku lomaliza la Allah **عَزَّوَجَلَّ**. Aliyense awerenga bukuli ndi kutsatira bwino lomwe adzapambana m'moyo wake wa padziko pano komanso omwe uli nkudza. **اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ عَزَّوَجَلَّ!** Dawat-e-Islami, ndi bungwe loima palokha lomwe silitenga mbali pa nkhani za ndale, koma limaphunzitsa Qur'an ndi Sunnah, ndipo linakhazikitsa nthambi zosiyanasiyana zosawerengeka (Madāris) [Sukulu za chisilamu] monga Madrasa-tul-Madīnah ophunzitsa Hifz [kuloweza Qur'an pa mtima] komanso Nāzirah [kuwerenga Qur'an poyang'ana] ku Pakistan ndi m'maiko ena. Panthawi yomwe tikulemba bukuli, ana okwana 75,000 akuphunzira ulere maphunziro a Hifz ndi Nāzirah ku Pakistan kokha. Sukulu zimenezi (Madāris), chidwi chimaikidwa pa maphunziro a chisilamu komanso kulera ana m'nyengo yomwe akuphunzira Qur'an yoyera, kuti akamaliza maphunziro ku Madrasa-tul-Madīnah akhale ndichidziwitso cha chisilamu komanso akhale owerenga Qur'an yoyera moyenera ndicholinga choti iwo adzakhale Asilamu aluntha komanso wodziwa zambiri, wochita bwino, aulemu ndi amakhalidwe abwino, opanda zoipa, wokutha kusiyanitsa chabwino ndi choipa komanso woyesetsa mwachangu kuzikonza wokha ndi ena m'dziko la pansu.

Pamene ana akulembedwa m'makalasi a Qāidah akanali ang'ono, bukuli linapangidwa chifukwa cha luso lawo lanzeru komanso likufotokoza mitu yosiyana siyana yachipembedzo kuphatikiza **تَعَوُّذ** (Ta'awwuz), **تَسْمِيَّه** (Tasmiyyah), **شَاء** (Shānā) yaifupi komanso ma Du'ā osavuta, zikhulupiro zoyambirira, Malamulo ofunikira, Chidziwitso cha mabuku awumulungu, zambiri zoyambirira za Aneneri **عَلَيْهِمُ السَّلَام**, Masahaba wodalitsika **رَضِيَ اللهُ عَنْهُمْ** ndi ma Auliyā a Allah.

Kuperekedwa kwa ziphunzitso zoyambirira za chisilamu (gawo-1) ndi mgwirizano wa Madrasa-tul-Madīnah ndi Al-Madīna-tul-'Ilmiyyah, pomwe kuwunikidwa kwa Sha'ria kwachitidwa ndi Dar-ul-Iftā Ahl-e-Sunnat.

Yihithay ārzūTa'līm-e-Quran 'ām hō jāye

Har aik parcham say aunchā parcham Islamhō jāye

Ziphunzitso za Qur'an zifalikire pa dziko lonse

Mulole mbendera ya chisilamu iwuluke pamwamba kuposa mbendera zina zonse

Majlis Madrasa-tul-Madīnah ndi Majlis Al-Madīna-tul-'Ilmiyyah

Lamasuliridwa m'chichewa ndi: Majlis-e-Tarajim

Hamd BariTa'ala

*TūhīMālik-e-baḥr-o-bar ḥayYāAllahuYā Allah
TūhīKhāliq-e-jinn-o-basharḥayYāAllahuYāAllah*

*TūAbadiḥayTūAzaliḥayTayrānām 'Alīm-o-'Alī ḥay
Zāt Tayrī sab say bar-tar ḥayYāAllahuYāAllah*

*Wasf bayān kartay ḥayn sārāy sang-o-shajar aur chānd sitāray
Tasbīḥḥarkhushk-o-tar ḥayYāAllahuYāAllah*

*Tayrācharchāgalīgalīḥaydālīdālīkalīkalīḥay
Wāṣifḥaraīkphūl-o-šamarḥayYāAllahuYāAllah*

*Khalqat jab pānī ko tar-say rim jḥim rim jḥimbarkhā bar-say
Ḥaraīk par RaḥmatkīnazarḥayYāAllahuYāAllah*

*Rāt nay jab sarapnāchūpāyāchiṛyaun nay yehzīkrsunāyā
Naghmahbārnasīm-e-saḥarḥayYāAllahuYāAllah*

*Bakhsh day Tū 'Aṭṭār ko Maulā wāsiṭah Tujḥ ko us piyāray kā
Jo kahNabiyaunkā Sarwar ḥayYāAllahuYāAllah*

(Wasāil-e-Bakhshish, .samba 42)

Na'at-e-Mustafa ﷺ

Ānkhaunkātārānām-e-Muhammad ﷺ
Dil kā ujālā nām-e-Muhammad ﷺ

Dawlat jo chāho dauno jahān kī
Kar lo waẓīfaḥnām-e-Muhammad ﷺ

Nūḥ-o-Khalīl-o-Mūsā-o-‘Īsā
Sab kā ḥay Āqā nām-e-Muhammad ﷺ

Pāyaīn murādayn dauno jahān mayn
Jis nay pukārā nām-e-Muhammad ﷺ

PūchaygāMaulālayāḥaykyākyā
Mayn yeḥ kahūn gā nām-e-Muhammad ﷺ

Apnay Razā kay qurbān jāon
Jis nay sikhāyā nām-e-Muhammad ﷺ

ApnayJamīlRizwī kay dilmayn
Ājā samā jā nām-e-Muhammad ﷺ

(Maddah-e-Ḥabīb Shaykh MaulānāJamīl-ur-RaḥmānRazavi رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ)

Azkār

Ṣalāh

Šanā

سُبْحَانَكَ اللَّهُمَّ وَبِحَمْدِكَ
وَتَبَارَكَ اسْمُكَ وَتَعَالَى جَدُّكَ وَلَا إِلَهَ غَيْرُكَ ط

Kumasulira:

Ulemerero kwa Inu, Ya Allah; nditamanda inu, dzina Lanu ndi Lodalitsika, Ukulu ndi ulemelero kwa Inu m'mwambamwamba ndipo palibe wina woyenera kupembezedwa kupatula Inu.

Ta'awwuz

أَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ ط

Kumasulira:

Ndikudzitchinjiriza kwa Allah kuchokera kwa Satana, wotembereredwa.

Tasmiyyah

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ ط

Kumasulira:

Ndiyamba ndi dzina la Allah, Wachifundo, Wachisoni chambiri.

Kalimāt (Ndemanga za chikhulupiriro)

Kalimah̄ Ṭayyibah̄

لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ مُحَمَّدٌ رَّسُولُ اللَّهِ ط

Kumasulira:

Palibe woyenera kupembedzedwa kupatula Allah, Muhammad ﷺ ndi Mneneri wa Allah.

Kalimah̄ Shaḥādat

أَشْهَدُ أَنْ لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَحْدَهُ لَا شَرِيكَ لَهُ وَأَشْهَدُ أَنَّ مُحَمَّدًا عَبْدُهُ وَرَسُولُهُ ط

Kumasulira:

Ndikuikira umboni kuti palibe wina woyenera kupembedzedwa mwa choonadi koma Allah yekha. Iye ndi wayekha ndipo alibe wophatikizana naye, ndikuikiranso umboni kuti Muhammad ﷺ ndi kapolo (Wosankhika) komanso Mneneri Wake.

Kalimah̄ Tamjīd

سُبْحَانَ اللَّهِ وَالْحَمْدُ لِلَّهِ وَلَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ وَاللَّهُ أَكْبَرُ وَلَا حَوْلَ وَلَا قُوَّةَ إِلَّا بِاللَّهِ الْعَلِيِّ الْعَظِيمِ ط

Kumasulira:

Ulemerero ukhale kwa Allah ndi matamando onse akhale kwa Allah ndipo palibe wina woyenera kupembedzedwa kupatula Allah, ndipo Allah ndi Wamkulu, palibe mphavu yopewera machimo komanso kuthekera kochita zabwino, koma kuchokera kwa Allah yemwe ndi wapamwambamwamba wamkulu koposa.

Şalat-‘Alan-Nabī ﷺ

Mneneri Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, ‘Kulikonse kumene muli ndifunireni ine zabwino pakuti zabwino zomwe mumandifunira zimandipeza.’ (*Sunan Abī Dāwūd, Kitāb-ul-Manāsik, Bāb: Ziyārat-il-Qubūr, Vol. 2, samba. 315, Hadīš 2042*)



صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ



الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَيْكَ يَا رَسُولَ اللَّهِ

Salat ndi Salam zikhale kwa Inu, E! Rasul wa Allah

وَعَلَى أَلِيكَ وَأَصْحَابِكَ يَا حَبِيبَ اللَّهِ

Komanso akubanja kwanu ndi Masahaba anu, E! wokondedwa wa Allah

الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَيْكَ يَا نَبِيَّ اللَّهِ

Salat ndi Salam zikhale kwa Inu, E! Mneneri wa Allah

وَعَلَى أَلِيكَ وَأَصْحَابِكَ يَا نُورَ اللَّهِ

Komanso akubanja kwanu ndi Masahaba anu, E! Nur wa Allah

Ma Du'ā

Du'ā tisanayambe kuwerenga Qur'an

أَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ ط

Kumasulira:

Ndikudzitchinjiriza kwa Allah kuchokera kwa Satana wotembereredwa.




Du'ā yonena popita kumalo okwera

اللَّهُ أَكْبَرُ ط

Kumasulira:

Allah ndi Wamkulu kwambiri.



Du'ā yonena pochoka malo okwera kupita ku malo otsika

سُبْحَانَ اللَّهِ ط

Kumasulira:

Ulemerero upite kwa Allah.



Du'ā yonena musanamwe madzi

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ ط

Kumasulira:

ndiyamba ndi dzina la Allah, Wachisoni, Wachifundo chambiri



Du'ā yonena mukamaliza kumwa madzi

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ ط

Kumasulira:

Matamando onse akhale kwa Allah, Rab wa maiko onse.



Du'ā yonena musanayambe kudya chakudya

بِسْمِ اللَّهِ وَعَلَى بَرَكَاتِهِ ط

Kumasulira:

Ndiyamba ndi dzina la Allah, ndi m'dalitso wa Allah ndidya.



Du'ā yonena mukamaliza kudya chakudya

الْحَمْدُ لِلَّهِ الَّذِي أَطْعَمَنَا وَسَقَانَا وَجَعَلَنَا مُسْلِمِينَ ط

Kumasulira:

ndikuthokoza Allah wa mphamvu zonse yemwe watipatsa ife chakudya ndi chakumwa ndipo watipanga ife Asilamu

(Sunan Abī Dāwūd, Kitāb-ul-Aṭ'imaḥ, Vol. 3, samba. 513, Ḥadīṣ 3850)



Du'ā yonena musanagone

اللَّهُمَّ بِأَسْبِكَ أَمُوتُ وَأَحْيِي ط

Kumasulira:

E Allah! Ndi dzina Lanu ndimwalira ndi kuzutsidwanso (mwachitsanzo kugona ndi kudzuka)

(Ṣaḥīḥ Bukhārī, Kitāb-ud-Da'wat, vol. 4, samba. 193, Ḥadīṣ 6314)

Du'ā yonena pamene mwadzuka ku tulo.

الْحَمْدُ لِلَّهِ الَّذِي أَحْيَانَا بَعْدَ مَا أَمَاتَنَا وَإِلَيْهِ النُّشُورُ ط

Kumasulira:

matamando onse apite kwa Allah amene watitsitsimutsa ife (kutidzutsa) pambuyo pa imfa (tulo), ndipo kwa iye tidzabwerera

(Al-Marja'-us-Sābiq)



Du'ā yonena pamene mwakumana ndi msilamu.

السَّلَامُ عَلَيْكُمْ وَرَحْمَةُ اللَّهِ وَبَرَكَاتُهُ ط

Kumasulira:

Mtendere ndi madalitso a Allah akhale pa inu.

Du'ā yonena pogwirana chanza ndi ena.

يَغْفِرُ اللَّهُ لَنَا وَلَكُمْ ط

Kumasulira:

Allah akhululukire inu ndi ine



Du'ā yothokozera wina.

جَزَاكَ اللَّهُ خَيْرًا ط

Kumasulira:

Allah akupatseni mphoto yabwino.



Zikhulupiriro

Chikhulupiriro komanso mitundu ya kafotokozedwe kake

Funso 1: Chikhulupiriro ndichani?

Yankho: Ndikukhulupirira m'malamulo komanso ziphunzitso zonse zimene Mneneri Muhammad صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anatibweletsera kuchokera kwa Allah عَزَّوَجَلَّ komanso ndikubvomereza zonsezi ndi mtima onse, chimenechi ndicho chikhulupiriro.

Funso 2: kodi mitundu ya kafotokozedwe ka chikhulupiriro ndi iti? Ifotokozeni

Yankho: pali mitundu iwiri ya kafotokozedwe ka chikhulupiriro:

(1) Īmān-e-Mujmal (2) Īmān-e-Mufaṣṣal

Funso 3: 'Īmān-e-Mujmal' ndi chiyani?

Yankho: Kufotokoza mwachidule za chikhulupiriro kumatchedwa 'Īmān-e- Mujmal

Funso 4: Werengani mokweza Īmān-e-Mujmal ndi Kutanthauza kwake.

Yankho:

Īmān-e-Mujmal

أَمِنْتُ بِاللَّهِ كَمَا هُوَ بِأَسْمَائِهِ
وَصِفَاتِهِ وَقَبِلْتُ جَمِيعَ أَحْكَامِهِ إِفْرَارًا بِاللِّسَانِ وَتَصْدِيقًا بِالْقَلْبِ ط

Kumasulira:

Ndikutsimikiza komanso ndikulengeza chikhulupiriro changa mwa Allah pakuti Iye ali ndi mayina Ake onse ndi Makhaliidwe, komanso ndikuvomeleza

(kumvera) malamulo ake onse, ndikulonjeza ndi lilime langa komanso ndikutsimikizira ndi mtima wanga.

Funso 5: Īmān-e-Mufaṣṣal ndichani?

Yankho: kufotokoza mwatsatanetsatane za chikhulupiriro kumatchedwa ‘Īmān-e-Mufaṣṣal’.

Funso 6: Werengani mokweza Īmān-e-Mufassal ndi Kutanthauza kwake.

Yankho:

Īmān-e-Mufassal

أَمَنْتُ بِاللَّهِ وَمَلَائِكَتِهِ وَكُتُبِهِ وَرُسُلِهِ
وَالْيَوْمِ الْآخِرِ وَالْقَدَرِ خَيْرِهِ وَشَرِّهِ مِنَ اللَّهِ وَالْبَعْثِ بَعْدَ الْمَوْتِ ط

Ndikukhulupirira mwa Allah, Angelo ake, ma Buku ake (ovumbulutsidwa), Aneneri ake, ndi tsiku la chiweruzo ndipo (ndikhulupirira kuti) tsogolo labwino ndi loyipa limachokera kwa Allah ndipo (ndikhulupirira kuti) kudzakhala chiukitso pambuyo pa imfa.

Zisanu Patsogolo pa Zisanu

Okonedwa ana! Ndithudi, moyo ndi waufupi kwambiri. Nthawi yomwe takhalapo siidzabweranso, ndipo chiyembekezo chilichonse chokhala ndi nthawi mtsogolo changokhala chinyengo chifukwa sitikudziwa chomwe chidzachitike kwa ife mtsogolo. Mwina tikhoza kumwalira nthawi yotsatira. Mtumiki Wokonedwa ndi Wodaltsika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wafotokoza kuti ‘Yang’anirani zinthu zisanu patsogolo pa zinthu zisanu: (1) Unyamata patsogolo pa ukalamba (ukalamba usanafike) (2) Thanzi patsogolo pa kudwala (3) Chuma patsogolo pa umphaŵi (4) Kupuma patsogolo pa kutanganidwa [kukhala otanganidwa]. (5) Moyo patsogolo pa imfa (imfa isanafike) (*Al-Mustadrak, vol. 5, p. 435, Ḥadīṣ 7912, Dar-ul-Ma’rifah, Beirut*)

Allah



Funso 1: Analenga ife ndani?

Yankho: Allah ﷻ anatilenga ife.

Funso 2: Ndi ndani yemwe analenga dziko lapansi, mlengalenga, dzuwa, mwezi ndi nyenyezi?

Yankho: Dziko lapansi, Mlengalenga, Dzuwa, Mwezi ndi Nyenyezi zinalengedwa ndi Allah ﷻ.

Funso 3: Timalambira ndani?

Yankho: Timalambira Allah ﷻ.

Funso 4: Ndani amamvetsera ndi kuwona chilichonse?

Yankho: Allah ﷻ ndiamene amamvetsera ndi kuwona chilichonse.

Funso 5: Kodi chilichonse chingabisike kwa Allah ﷻ?

Yankho: Ayi! Palibe chomwe chingabisike kwa Allah ﷻ. Iye amadziwa chilichonse.

Mneneri wathu Wokonedwa ﷺ



Funso 1: Dzina Lodala la Mneneri wathu Wokonedwa ﷺ ndi liti?

Yankho: Dzina Lodala la Mneneri wathu Wokonedwa ﷺ ndi Muhammad ﷺ.

Funso 2: kodi Mneneri wathu Wokonedwa ﷺ anabadwira mzinda uti?

Yankho: Mneneri wathu Wokonedwa ﷺ anabadwila ku Makka-tul-Mukarramah, mzinda wotchuka waku Arabia.

Funso 3: Kodi ndi tsiku liti komanso mwezi uti womwe Mneneri Wokonedwa ﷺ anabadwa?

Yankho: Mneneri wathu Wokonedwa ﷺ anabadwa pa 12 mwezi wa Rabī-ul-Awwal.

Funso 4: Ndi tsiku liti lomwe Mneneri wathu Wokonedwa ﷺ anabadwa?

Yankho: Wokonedwa Mtumiki ﷺ anabadwa lolemba.

Ziphunzitso za chisalamu zoyambilira

Funson 5: Dzina la bambo a Mneneri wathu Wokonededwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi ndani?

Yankho: Dzina la bambo a Mneneri wathu Wokonededwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi Sayyidunā ‘Abdullāh رَضِيَ اللهُ عَنْهُ.

Funson 6: Dzina la mayi a Mneneri wathu Wokonededwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi ndani

Yankho: Dzina la mayi a Mneneri wathu Wokonededwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi Sayyidatunā Āminah رَضِيَ اللهُ عَنْهَا.

Funso 7: Manda opatulika odala a Mneneri wathu Wokonededwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ali kuti?

Yankho: Manda opatulika odala a Mneneri wathu Wokonededwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ali ku Madīna-tul-Munawwarah.

Funso 8: Zaka za Mneneri wathu Wokonededwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi zingati?

Yankho: Zaka za Mneneri wathu Wokonededwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi 63.

Chipembedzo chathu

Funso 1: Ndife yani pa chipembedzo?

Yankho: Ndife Asilamu pa chipembedzo.

Funso 2: Chipembedzo chathu ndi chani?

Yankho: Chipembedzo chathu ndi Chisilamu.

Funso 3: Msilamu ndi ndani?

Yankho: Yemwe akhulupirira Chisilamu ndi Msilamu.

Funso 4: Asilamu amapembedza ndani?

Yankho: Asilamu amapembedza Allah عَزَّوَجَلَّ yekha.

Funso 5: Chisilamu chimatiphunzitsa chani?

Yankho: Chisilamu chimatiphunzitsa, zowona, Ukhondo, ubwino ndi chilungamo.

Funso 6: Kalimah ya Chisilamu ndichani?

Yankho: Kalimah ya Chisilamu ndi:

لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ مُحَمَّدٌ رَّسُولُ اللَّهِ ﷺ

Palibe wina woyenera kupembedzedwa kupatula Allah, ndipo Muhammad ndi Mneneri wa Allah.



Nsanamira za chisilamu

Funso 1: Chisilamu chili ndi nsanamira zingati?

Yankho: Chisilamu chili ndi nsanamira zisanu, : (1) Kuchitira umboni kuti palibe wina woyenera kupembedzedwa kupatula Allah عَزَّوَجَلَّ, Ndipo Muhammad صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi Mtumiki Wolemekezeka komanso Mneneri wa Allah عَزَّوَجَلَّ. (2) Kupemphera Salah (3) Kupereka Zakāh (4) Kuchita Hajj (5) Kusala kudya mwezi wa Ramaḍān. (*Ṣaḥīḥi Bukhārī, Kitāb-ul-Īmān, Vol. 1, samba. 14, Ḥadīṣ 8*)

Funso 2: Ndi mapemphero angati ali Fard (okakamiza) mu usana ndi usiku?

Yankho: Mapemphero a fard (okakamizidwa) alipo asanu.

Funso 3: Tchulani maina asanu a mapemphero a Fard.

Yankho: (1) Fajr (2) Zūhr (3) ‘Aṣr (4) Maghrib (5) ‘Ishāh

Funso 4: Ndi mwezi uti omwe ndi zokakamizidwa (Fard) kuti Asilamu azisala kudya?

Yankho: Ndi Fard kwa Asilamu kusala m’ mwezi wodala wa Ramadan.

Funso 5: Hajj ndi Fard kwa ndani?

Yankho: Hajj ndi Farḍ kamodzi, m’ moyo wonse, kwa Msilamu aliyense amene ali ndi kuthekera kuyichita.

Funso 6: Ndikuti komwe Hajj imachitikira?

Yankho: Hajj imachitikira ku Makka-tul-Mukarramah.

Angelo

Funso 1: Angelo ndi ndani?

Yankho: Angelo ndi zolengedwa za Allah ﷺ ndipo analengedwa kuchokera ku Nur (kuwala).

Funso 2: Kodi angelo amatani?

Yankho: Angelo amachita ndendende zomwe Allah ﷻ walamula.

Funso 3: Mtsogoleri wa Angelo onse ndi ndani?

Yankho: Mtsogoleri wa Angelo onse ndi Jibril عَلَيْهِ السَّلَام.

Funso 4: Chiwerengero chonse cha Angelo ndi chokwana bwani?

Yankho: Allah yekha ﷺ ndi Mneneri wake صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi amene akudziwa chiwerengero cha Angelo.

Funso 5: Angelo amadya ndi kumwa chani?

Yankho: Angelo sadya kapena kumwa chilichonse.

Paradizo ili pansi pa mapazi amayi

Sayyidunā Anas bin Mālik رَضِيَ اللهُ عَنْهُ anafotozoza kuti Mneneri wa anthu, mtendere wa m'mtima mwathu komanso malingaliro athu, wopatsa kwambiri ndi wokoma mtima, صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, 'Paradizo wagona pansi pa mapazi amayi.' (*Kanz-ul-Ummāl, Kitāb-un-Nikah, Vol. 16, samba. 192, Ḥadīṣ 45431*)

Aneneri عَلَيْهِمُ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ



Funso 1: Mneneri ndi ndani?

Yankho: Munthu yemwe Allah عَزَّوَجَلَّ amamutumizira vumbulutso lotsogolera amatchedwa Mneneri.

Funso 2: Ndi Mneneri uti عَلَيْهِ السَّلَامُ yemwe Allah عَزَّوَجَلَّ anamulenga koyambirira?

Yankho: Allah عَزَّوَجَلَّ analenga Sayyidunā Ādam عَلَيْهِ السَّلَامُ koyambirira.

Funso 3: Mneneri womaliza kutumizidwa pa dziko ndi ndani?

Yankho: Mneneri womaliza kutumizidwa pa dziko lapansi ndi Mneneri wathu Wokonedwa Muhammad Mustafa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ.

Funso 4: Pambuyo pa Mneneri wathu Wokonedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ , kodi pali Mneneri yemwe angabwelenso mu dziko lapansi?

Yankho: Palibe Mneneri yemwe angabwele pa dziko lapansi pambuyo pa Mneneri wathu Wokonedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ.

Funso 5: Ngati wina anena zabodza kuti ndi Mtumiki amatchedwa ndani?

Yankho: Ngati wina anena zabodza kuti ndi Mtumiki amatchedwa, ‘Kazzāb (wabodza wamkulu)’.

Funso 6: Kodi aneneri onse عَلَيْهِمُ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ ali ndi moyo m’manda mwawo?

Yankho: Inde!

Funso 7: Wamkulu wa Aneneri onse عَلَيْهِمُ الصَّلَامُ ndi ndani?

Yankho: Wamkulu wa Aneneri onse ndi Mneneri wathu Wokonedwa Muhammad Mustafa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ.

Funso 8: **Tanthauzo la** mawu oti Mneneri A’lā Ḥaḍrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anafotokoza motani mu Kanz-ul-Īmān?

Yankho: ‘Yemwe amafotokoza nkhani za Ghayb [zobitsika].’

Funso 9: Tchulani maina ena a Aneneri عَلَيْهِمُ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ.

Yankho:

1. Sayyidunā Adam عَلَيْهِ السَّلَامُ	4. Sayyidunā Nūḥ عَلَيْهِ السَّلَامُ
2. Sayyidunā Mūsā عَلَيْهِ السَّلَامُ	5. Sayyidunā ‘Īsā عَلَيْهِ السَّلَامُ
3. Sayyidunā Dāwūd عَلَيْهِ السَّلَامُ	6. Sayyidunā Sulaymān عَلَيْهِ السَّلَامُ
7. Mneneri wathu Wokonedwa Muhammad Mustafa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ.	

Mu'jizāt (Zozizwitsa) za Aneneri عَلَيْهِمُ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ

Funso 1: Mu'jizāh [Chozizwa] ndi chani?

Yankho: Mchitidwe wauzimu wa Mneneri ochitidwa atatha kulengeza za uneneri wake umatchedwa Mu'jizāh.

Funso 2: Ndi mneneri uti عَلَيْهِ السَّلَامُ amene amasintha chitsulo kukhala chofewa ngati sera pamene wachinyamula m'manja mwake?



Yankho: Sayyidunā Dāwūd عَلَيْهِ السَّلَامُ akanyamula chitsulo m'manja mwake, chimasintha kukhala chofewa ngati sera.

Funso 3: Ndi mneneri uti عَلَيْهِ السَّلَامُ amene anapanga njira pa mtsinje pomenya ndi ndodo yake pa madzi a m'mtsinje?



Yankho: Sayyidunā Mūsā عَلَيْهِ السَّلَامُ anapanga njira pa mtsinje pakumenya madzi a m'mtsinje ndi ndodo yake.

Funso 4: Ndi mneneri uti عَلَيْهِ السَّلَامُ yemwe anamwetulira atamva phokoso la nyerere kuchokera pa mamailosi atatu?



Yankho: Sayyidunā Sulaymān عَلَيْهِ السَّلَامُ anamwetulira atamva phokoso la nyerere kuchokera pa mamayilosi atatu.

Funso 5: Ndi Mneneri uti amene anali ndi Ngamila yaikazi ya m'paradiso yomwe imatha kumwa madzi onse a m'dziwe pa nthawi yake?



Yankho: Sayyidunā Šālih عَلَيْهِ السَّلَامُ ndi amene anali ndi Ngamira yaikazi ya m'paradizo yomwe imamwa madzi onse a m'dziwe pa nthawi yake.

Mabuku omwe anavumbulutsidwa.

Funso 1: Ndi mabuku ati amene amatchedwa ovumbulutsidwa?

Yankho: Mabuku a Allah ﷺ amatchedwa mabuku ovumbulutsidwa.

Funso 2: Mabuku amenewa anavumbulutsidwa kwa ndani?

Yankho: Mabuku amenewa anavumbulutsidwa kwa Aneneri عَلَيْهِمُ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ.

Funso 3: Chifukwa chiyani mabukuwa anavumbulutsidwa?

Yankho: Mabukuwa anavumbulutsidwa kuti awongolere anthu.


Funso 4: Ndi mabuku ati ovumbulutsidwa omwe ndi wodziwika?

Yankho: (1) Tawrāt (2) Zabūr (3) Injil (4) Quran

Khalidwe lotchuka la Chisilamu

Kufunika kwakukulu ndi kudzichepetsa mu Chisilamu. Zanenedwa mu Ḥadīṣ, ‘Inde, Chipembedzo chilichose chile ndi khalidwe ndipo khalidwe la Chisilamu ndi kudzichepetsa.’ (*Sunan Ibn Mājah, Vol. 4, samba. 460, Ḥadīṣ 4181; Dār-ul-Maʿrifah, Beirut*) Mwanjira ina, Ummah uliwonse uli ndikhalidwe limodzi lomwe ndilodziwika kwambiri kuposa makhalidwe ake ena, ndipo khalidwe lotchuka la Chisilamu ndiko kudzichepetsa.

Maswahaba عَلَيْهِمُ الرِّضْوَان



Funso 1: Ndani amatchedwa Swahaba?

Yankho: Swahaba ndi yemwe ali ndi Iman anawona Mneneri Wokonedwa ndi Wodala صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ komanso anamwalira ali ndi Iman.

Funso 2: Ndi maswahaba ati wotchedwa Khulafā-e-Rāshidīn?

Yankho: maswahaba anayi a Mneneri صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ womwe anakhala makhalifa woyambirira pambuyo pa imfa ya Mneneri صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ amatchedwa Khulafā-e-Rāshidīn.

Funso 3: Tchulani maina ama Khulafā-e-Rāshidīn.

Yankho:

- ❖ Amīr-ul-Mūminīn Sayyidunā Abū Bakr Ṣiddīq رَضِيَ اللهُ عَنْهُ.
- ❖ Amīr-ul-Mūminīn Sayyidunā ‘Umar Fārūq A’ẓam رَضِيَ اللهُ عَنْهُ.
- ❖ Amīr-ul-Mūminīn Sayyidunā ‘Uṣmān Ghānī رَضِيَ اللهُ عَنْهُ.
- ❖ Amīr-ul-Mūminīn Sayyidunā ‘Alī-ul-Murtaḍā رَضِيَ اللهُ عَنْهُ.

Funso 4: Nenani maina a maswahaba ena a Mneneri Woyera
صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ.

Yankho: Maina a maswahaba ena a Mneneri Woyera
صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ ndi:

- ❖ Sayyidunā ‘Abdullāh Bin ‘Abbās رَضِيَ اللهُ عَنْهُمَا.
- ❖ Sayyidunā ‘Abdullāh Bin ‘Umar رَضِيَ اللهُ عَنْهُمَا.
- ❖ Sayyidunā ‘Abdullāh Bin Mas’ūd رَضِيَ اللهُ عَنْهُ.
- ❖ Sayyidunā Amīr Mu’āwiyah رَضِيَ اللهُ عَنْهُ.
- ❖ Sayyidunā Imām Ḥasan رَضِيَ اللهُ عَنْهُ.
- ❖ Sayyidunā Imām Ḥusain رَضِيَ اللهُ عَنْهُ.

Bzalani mtengo M’paradizo

Wokonedwa ana! Mutha kuzindikira ubwino wa nthawi, komanso pamene tikukhala m’dziko la pansi titha kukhala ndi mtengo obzalidwa ndi inu mu paradizo ka mphindi kochepa! Kukhala ndi mtengo obzalidwa m’paradizo ndi kosavuta. Malingana ndi Ḥadiṣ, inatchulidwa mu Ibn Mājah, ‘Mtengo udzabzalidwa m’paradizo kwa amene angawerenge mawu mwa anayi awa:

(1) سُبْحَانَ اللَّهِ (2) الْحَمْدُ لِلَّهِ (3) لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ (4) اللَّهُ أَكْبَرُ

(Sunan Ibn-e-Mājah, Vol. 4, p. 252, Ḥadiṣ 3807, Dār-ul-Ma’rifah, Beirut)

Auliya Allah رَحْمَهُمُ اللَّهُ السَّلَام



Funso 1: Ndi ndani amatchedwa waliyullāh (Bwenzi la Allah عَزَّوَجَلَّ)?

Yankho: Msilamu yemwe wasiya zokhumba zake ndi kudzipereka kwa Allah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ komanso kwa Mneneri Wake عَزَّوَجَلَّ nithawi zonse, amatchedwa Waliyullāh.

Funso 2: Nenani maina a ena mwa Auliya a Allah رَحْمَهُمُ اللَّهُ komanso nenani komwe manda awo opatulika ali?

Yankho: Molingana ndi makomo 8 aku Paradizo, nawa maina ama Auliya Allah okwana 8 ndi maina a mizinda komwe kuli manda awo opatulika.

- ❖ Sayyidunā Shaykh ‘Abdul Qādir Jīlānī (Ghauṣ-e-A’ẓam رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ): Manda ake opatulika ali ku Baghdad, Iraq.
- ❖ Sayyidunā Mu’īnuddīn Chishtī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ: manda ake opatulika ali ku Ajmer, India.
- ❖ Sayyidunā Shaykh Shāhābuddīn Suhāwardī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ: manda ake

opatulika ali ku Suhrward, Iran.

- ❖ Sayyidunā Shaykh Bahāuddīn Naqshband بَرَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ: Manda ake opatulika ali ku Bukhara, Uzbekistan.
- ❖ Sayyidunā ‘Alī Ḥajwaīrī (Dātā Ganj Bakhsh) بَرَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ: Manda ake opatulika ali ku Markaz-ul-Auliya Lahore, Pakistan.
- ❖ Sayyidunā Bahāuddīn Zikriyāḥ Multānī بَرَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ: Manda ake opatulika ali ku Madina-tul-Auliya Multan, Pakistan.
- ❖ Sayyidunā Bābā Farīduddīn Ganj Shakar بَرَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ: Manda ake opatulika ali ku Pakpattan, Pakistan.

Sayyidunā Imām Ahl-e-Sunnat Maulana Shah Imām Ahmad Razā Khān بَرَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ: Manda ake opatulika ali ku Bareilly, India.

Ukhondo

Mneneri Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati: Ukhondo nditheka la chikhulupiriro.

(Ṣaḥīḥ Muslim, Kitāb-ut-Ṭahārat, p. 140, Ḥadīṣ 223)

Machitidwe a kulambira

Wudū



Funso 1: Ndi ma Farāiḍ (zikakamizo) ati komanso ndi angati omwe ali mu Wuḍū?

Yankho: Pali ma Farāiḍ anayi mu Wuḍū:

1. Kusambitsa nkhope.
2. Kusamba mikono yonse mpaka muchigongono.
3. Kudutsitsa dzanja lonyowa mu gawo limodzi mwa magawo anayi a pamutu panu.
4. Kusambitsa mapazi onse mpaka mumisomali. (*Namāz key Ahkām, samba. 14*)

Funso 2: Tiyenera kuwerenga chani tisanapange Wuḍū?

Yankho: Ndi Sunnah kuwerenga بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ musanapange Wuḍū.

Funso 3: Kodi ubwino wowerenga بِسْمِ اللّٰهِ ndi wotani musanapange Wuḍū?

